# Maphunziro a m’Baibulo

Bible studies

# Malamulo Khumi a Mulungu

1. Malamulo Khumi a Mulungu
2. Fano la mwana wa ng’ombe

# 1. Malamulo Khumi a Mulungu

**Eksodo 19.1-9**

1. Mwezi wacitatu ataturuka ana a Israyeli m'dziko la Aigupto, tsiku lomwelo, analowa m'cipululu ca Sinai.
2. Pakuti anacoka ku Refidimu, nalowa m'cipululu ca Sinai, namanga tsasa m'cipululumo; ndipo Israyeli anamanga tsasa pamenepo pandunji pa phirilo.
3. Ndipo Mose anakwera kwa Mulungu; ndipo Yehova ali m'phirimo anamuitana, ndi kuti, Uzitero kwa mbumba ya Yakobo, nunene kwa ana a Israyeli, kuti,
4. Inu munaona cimene ndinacitira Aaigupto; ndi kuti ndanyamula inu monga pa mapiko a mphungu, ndi kubwera nanu kwa Ine ndekha.
5. Ndipo tsopano, ngati mudzamvera mau anga ndithu, ndi kusunga cipangano canga, ndidzakuyesani cuma canga ca padera koposa mitundu yonse ya anthu; pakuti dziko lonse lapansi ndi langa;
6. ndipo ndidzakuyesani ufumu wanga wa ansembe, ndi mtundu wopatulika. Awa ndi mau amene ukalankhule ndi ana a lsrayeli.
7. Ndipo Mose anadza, naitana akuru a anthu, nawaikira pamaso pao mau awa onse amene Yehova adamuuza.
8. Ndipo anthu onse anabvomera pamodzi, nati, Zonse adazilankhula Yehova tidzazicita. Ndipo Mose anabwera nao mau a anthu kwa Yehova.
9. Ndipo Yehova anati kwa Mose, Taona, ndikudza kwa iwe mu mtambo wakuda bii, kuti anthu amve pamene ndilankhula ndi iwe, ndi kuti akubvomereze nthawi zonse. Pakuti Mose adauza Yehova mau a anthuwo.

**Eksodo 19.16-20**

16. Ndipo kunali tsiku lacitatu, m'mawa, panali mabingu ndi zimphezi, ndi mtambo wakuda bii paphiripo, ndi liu la lipenga lolimbatu; ndi anthu onse okhala kutsasa ananjenjemera.
17. Ndipo Mose anaturutsa anthu kutsasa, kuti akomane ndi Mulungu; ndipo anaima patsinde pa phiri.
18. Ndipo phiri la Sinai linafuka monsemo, popeza Yehova anatsikira m'moto pamenepo; ndi utsi wace unakwera ngati utsi wa m'ng'anjo, ndi phiri lonse linagwedezeka kwambiri,
19. Ndipo pamene liu la lipenga linamveka linakulira-kulira, Mose ananena, ndi Mulungu anamyankha ndi mau.
20. Ndipo Yehova anatsikira pa phiri la Sinai, pamutu pace pa phiri; ndipo Yehova anaitana Mose akwere pamutu pa phiri; ndi Mose anakwerapo

**Eksodo 20.1-21**

1. Ndipo Mulungu ananena mau onse amenewa, nati:
2. INE ndine YEHOVA Mulungu wako, amene ndinaturutsa iwe ku dziko la Aigupto, ku nyumba ya akapolo.
3. Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.
4. Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena cifaniziro ciri conse ca zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko;
5. usazipembedzere izo, usazitumikire izo; cifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana cifukwa ca atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai wa iwo amene akudana ndi Ine;
6. ndi kuwacitira cifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga.
7. Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa, amene achula pacabe dzina lacelo.
8. Uzikumbukila tsiku la Sabata, likhale lopatulika.
9. Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza nchito zako zonse;
10. koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire nchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wanchito wako wamwamuna, kapena wanchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako;
11. cifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku ladsanu ndi ciwiri; cifukwa cace Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.
12. Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti acuruke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.
13. Usaphe.
14. Usacite cigololo.
15. Usabe.
16. Usamnamizire mnzako.
17. Usasirire nyumba yace ya mnzako, usasirire mkazi wace wa mnzako, kapena wanchito wace wamwamuna, kapena wanchito wace wamkazi, kapena ng'ombe yace, kapena buru wace, kapena kanthu kali konse ka mnzako.

18. Ndipo anthu onse anaona mabingu ndi zimphezi, ndi liu la lipenga, ndi phiri lirikufuka; ndipo pamene anthu anaziona, ananjenjemera, naima patali.
19. Ndipo anati kwa Mose, Mulankhule nafe ndinu, ndipo tidzamva; koma asalankhule nafe Mulungu, kuti tingafe,
20. Ndipo Mose anati kwa anthu, Musaope; pakuti Mulungu wadza kukuyesani ndi kuti kumuopa iye kukhale pamaso panu, kuti musacimwe.
21. Ndipo anthu anaima patali, koma Mose anayandikiza ku mdima waukuru kuli Mulungu.

**Mafunso**

1. Mulungu anafotokoza kuti Aisrayeli ndiwo anthu ake. Cifukwa cake iwo anayenera kusunga malamulo ake. Kodi anthu anayankha bwanji kulingana ndi Eksodo 19 ndime ya 8?
2. Nanga inu, mufunanso kucita zonse zimene Mulungu atilamulira m'Baibulo?
3. Ndi ciani cimene cinacitika pa tsiku lacitatu? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
4. Chulani dzina la phiri kumene Mulungu anapatsa malamulo ake. Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
5. Ganizirakoni Malamulo Khumi a Mulungu. Kodi mudziwa munthu amene saphwanya lamulo lirilonse poganiza, pocita ndi kunena?
6. Nanga inu nokha, mumasunga konse malamulo a Mulungu?
7. Baibulo likamba kuti, 'Ndi dziko lonse lapansi litsutsidwe ndi Mulungu' (Aroma 3.19b). Zocita zathu sizitipulumutsa ku macimo athu. Ndi cifukwa ciani tifunika Yesu Mpulumutsi?
8. Kodi anthu anamva bwanji atamva Malamulo Khumi? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
9. Nanga inu, mukumva bwanji m'mtima mwanu pamene mukumva Malamulo Khumi a Mulungu?

**Sewero**

Lembani malembo pa malo ao

Aroma 3.10b

| 16 | 1 | 13 | 1 | 19 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 16 | 1 | 3 | 5 |
|---|---|---|---|
| | | | |

| 16 | 1 | 12 | 9 | 2 | 5 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 13 | 21 | 14 | 20 | 8 | 21 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 1 | 4 | 26 | 1 | 25 | 5 | 19 | 5 | 4 | 23 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | | | |

| 23 | 15 | 12 | 21 | 14 | 7 | 1 | 13 | 1 |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | | | | |

| 14 | 4 | 9 |
|---|---|---|
| | | |

| 14 | 3 | 8 | 9 | 20 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| 26 | 1 |
|---|---|
| | |

| 12 | 1 | 13 | 21 | 12 | 15 |
|---|---|---|---|---|---|
| | | | | | |

| **1** | **2** | **3** | **4** | **5** | **6** | **7** | **8** | **9** | **10** | **11** | **12** | **13** |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| A | B | C | D | E | F | G | H | I | J | K | L | M |

| **14** | **15** | **16** | **17** | **18** | **19** | **20** | **21** | **22** | **23** | **24** | **25** | **26** |
|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|---|
| N | O | P | Q | R | S | T | U | V | W | X | Y | Z |

## 2. Fano la mwana wa ng'ombe

**Eksodo 32.1-20**

1. Koma pamene anaona kuti Mose anacedwa kutsika m'phiri, anthuwo anasonkhana kwa Aroni, nanena naye, Ukani, tipangireni milungu yakutitsogolera; pakuti Mose uyu, munthuyu anatikweza kucokera m'dziko la Aigupto, sitidziwa comwe camgwera.
2. Ndipo Aroni ananena nao, Thyolani mphete zagolidi ziri; m'makutu a akazi anu, a ana anu amuna ndi akazi, ndi kubwera nazo kwa ine.
3. Ndipo anthu onse anathyola mphete zagolidi zinali m'makutu mwao, nabwera nazo kwa Aroni.
4. Ndipo anazilandira ku manja ao, nacikonza ndi cozokotera, naciyenga mwana wa ng'ombe; ndipo anati, Siyi milungu yako, Israyeli, imene inakukweza kucokera m'dziko la Aigupto.
5. Pakuciona Aroni, anamanga guwa la nsembe patsogolo pace; ndipo Aroni anapfuula nati, Mawa aliko madyerero a Yehova.
6. Ndipo m'mawa mwace anauka mamawa, nafukiza nsembe zopsereza, nabwera nazo nsembe zamtendere; ndi anthu anakhala pansi kudya ndi kumwa, nauka kusewera.
7. Ndipo Yehova anati kwa Mose, Muka, tsikatu, pakuti anthu ako udakwera nao kucokera m'dziko la Aigupto wadziipsa;
8. wapatuka msanga njira imene ndinawauza; wadzinyengera mwana wa ng'ombe, namgwadira, namphera nsembe, nati, Siyi milungu yako, Israyeli, imene inakukweza kucokera m'dziko la Aigupto,
9. Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ndawapenya anthu awa, taona, ndiwo anthu opulupudza;
10. ndipo tsopano ndileke, kuti ndipse mtima pa awo ndi kuwatha, ndi kukuza iwe ukhale mtundu waukuru.
11. Ndipo Mose anapemba kwa Yehova Mulungu wace, nati, Yehova, mtima wanu upserenji pa anthu anu, amene munawaturutsa m'dziko la Aigupto ndi mphamvu yaikuru, ndi dzanja lolimba?
12. Akaneneranji Aaigupto; ndi kuti, Anawaturutsa coipa, kuti awaphe m'mapiri, ndi kuwatha pankhope pa dziko lapansi? Pepani, lekani coipaco ca  pa anthu anu.
13. Kumbukilani Abrahamu, Isake ndi Israyeli, atumiki anu, amene munawalumbirira ndi kudzichula nokha, amene munanena nao, Ndidzacurukitsa mbeu zanu ngati nyenyezi za kuthambo, ndi dziko ili lonse ndanenali ndidzapatsa mbeu zanu, likhale colowa cao nthawi zonse.
14. Ndipo Yehova analeka coipa adanenaci, kuwacitira anthu ace.

Mose atsikira anthu opembedza fanolo

15. Ndipo Mose anatembenuka, natsika m'phirimo, magome awiri a mboni ali m'dzanja lace; magome olembedwa kwina ndi kwina; analembedwa mbali yina ndi inzace yomwe.
16. Ndipo magomewo ndiwo nchito ya Mulungu, kulembaku ndiko kulemba kwa Mulungu, kozokoteka pa magomewo.
17. Ndipo pamene Yoswa anamva phokoso la kupfuula kwa anthu, anati kwa Mose, Kuli phokoso la nkhondo kucigono.
18. Koma iye anati, Phokosoli sindilo la kupfuula kwa olakika, kapena la kupfuula kwa opasuka; koma phokoso ndikumvali ndilo la othirirana mang'ombe.
19. Ndipo kunali, pamene anayandikiza cigono, anaona mwana wa ng'ombeyo ndi kubvinako; ndipo Mose anapsa mtima, nataya magome ali m'manja mwace, nawaswa m'tsinde mwa phiri.
20. Ndipo anatenga mwana wa ng'ombe anampangayo, namtentha ndi moto, nampera asalale, namwaza pamadzi, namwetsako ana a Israyeli.

**Eksodo 32.30-35**

30. Ndipo kunali m'mawa mwake, kuti Mose anati kwa anthu, Mwachimwa kuchimwa kwakukulu; koma ndikwera kwa Yehova tsopano, kapena ndidzachita chotetezera uchimo wanu.
31. Ndipo Mose anabwerera kumka kwa Yehova, nati, Ha! pepani, anthu awa anacimwa kucimwa kwakukuru, nadzipangira milungu yagolidi.
32. Koma tsopano, kapena mudzakhululukira kucimwa kwao; koma ngati mukana, mundifafanizetu, kundicotsa m'buku lanu limene munalembera,
33. Ndipo Yehova anati kwa Mose, iye amene wandicimwira, ndifafaniza yemweyo kumcotsa m'buku langa.
34. Ndipo tsopano, muka, tsogolera anthu kumka nao kumene ndinakuuza; taona, mthenga wanga akutsogolera; koma tsiku lakuwazonda Ine ndidzawalanga cifukwa ca kucimwa kwao.
35. Ndipo Yehova anakantha anthu, cifukwa anapanga mwana wa ng'ombe amene Aroni anapanga.

**Mafunso**

1. Kodi Aisrayeli anafuna ciani kulingana ndi ndime ya 1?
2. Kodi Aroni anacita ciani ndi mphete zagolide za Aisrayeli? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
3. Kodi Mulungu anakondwera pa kuona zimene Aisrayeli anacita? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?

4. Mulungu anafuna kuononga Aisrayeli cifukwa ca macimo ao (ndime ya 10). Ocimwa onse adzaonongeka ku Gehena. Kuli njira imodzi ya cipulumutso: Yesu. Kodi ndinu wopulumutsidwa ku macimo anu?
5. Kodi Mose anacita ciani atamva kuti Mulungu afuna kuononga Asirayeli? Ndi m'ndime iti mwapeza yankho?
6. Nanga inu mumacita ciani mutacimwira Mulungu?
7. Werenganinso ndime ya 30. Mose anacita cotetezera uchimo wa Aisrayeli. Kodi ndani amene akhoza ndi kufuna kucita cotetezera uchimo wathu?

**Sewero**

Pezani mau onse

| | | | | | |
|---|---|---|---|---|---|
| N | G | O | M | B | E |
| A | P | D | O | V | I |
| R | F | S | S | C | Z |
| O | G | U | E | A | I |
| N | K | W | A | N | R |
| I | R | W | O | A | I |
| B | A | N | P | W | H |
| L | A | N | A | M | P |
| F | C | H | I | M | O |
| M | P | H | E | T | E |

- fano
- mphete
- Aroni
- chimo
- mboni
- mwana
- Mose
- phiri
- ng'ombe
- kwa
- ana

**Nyimbo**

Kwa Inu Yesu ndilira,
Wopanda Inu ndidzafa;
Mupulumutse inedi,
Mundilandiretu.

*Mundilandiretu,*
*Ndiipa m'mtimamo;*
*Kotero mnandiferatu,*
*Mundilandiretu.*

Ndifoka ndi zoipazo,
Ndidzalatu ndi macimo.
Sinditha kuzitayazo;
Mundilandiretu

Ndayesa kudzikonzadi,
Ndapeza mphamvu ndilibe.
Zoipa zakanikadi;
Mundilandiretu.

Onani Mbuye ndigonja,
Kuyesa kwanga ndaleka;
Citani Inu mumtima;
Mundilandiretu.

Muyambe nchito yanuyi,
Musalekenso, chitani;
Ndidzipereka leroli;
Mundilandiretu.

**Nyimbo**

Ndisauka, ndinacimwa, koma Inu mwandifera;
Ndimo ndamva mund'itana, Mwana wa Mlungu, ndikubwera.

Ndisauka, ndimasowa, mphamvu ya kuyera m'mtima;
Mwazi wanu wanditsuka, Mwana Mlungu, ndikubwera.

Ndisauka, sindikhoza, kuiletsa nkhondo m'mtima;
Ndi cisoni, mantha, nkhawa, Mwana Mlungu, ndikubwera.

Ndisauka, sindiona, ndikudwala, ndilefuka;
Zonse ndizitaya kwa 'Nu, Mwana Mlungu, ndikubwera.

Inde, Yesu, mulandira, muciritsa, mupulumutsa;
Mau anu ndibvomera, Mwana Mlungu, ndikubwera.

Inde, Yesu, mundikonda, zonse zina ndazitaya;
Tsono kukakhala wanu, Mwana Mlungu, ndikubwera.